Saying, 'Although it created us, this issue is about worldly matters'
 Chabwino ndavomera, sindikambapo za Baibulo
Alright, I agree, I shall not talk about the Bible
 Ngakhalenso nalonso mwamvemve lidanena
Although it also says very clearly
 Kuti mathanyula ndi nyansi zenizeni pamaso pa Mulungu
That homosexuality is proper filth in God's eyes⁴

Munakhala bwanji inu, kuipa moyo kumeneku bwanji?
How come you are like that, wishing others ill?
 Nthawi zonse kampeni kumphasa ndi ife
Every time plotting against us⁵
 Pansi mtedza Malawi
Malawi, be alert!⁶

¹*Mtereshi* and *tofu* are slang expressions for 'money' (*ndalama*); they are less common than *makobidi*, which the poet chooses not to use.

²Being 'light-skinned' (*kuyera khungu*) is considered desirable in Malawi, and its rejection is an early sign of defiance in the poem.

³When money is *nyansi*, it is 'dirty', not only for its illicit or immoral aspects, but also because it is repulsive in a visceral sense.

⁴*Nyansi* is translated here as 'filth'.

⁵*Kampeni kumphasa* is a common idiom for plotting and evokes 'a small knife' (*kampeni*) hidden under 'a mat' (*mphasa*).

⁶*Pansi mtedza* is an idiomatic command that urges vigilance against an impending threat. It literally asks to 'hide the groundnuts' and was used in this sense to warn against marauders.

Bwenzi ili ndi lachiphamaso
*This friendship is hypocritical*⁷
 Zolowere nkudyere mwana ndiye uyu
*Familiarity with that one results in eating a child*⁸

Unkati ndiwe bwenzi pobweranso utathamangitsidwa ngati mtsamunda
*You were saying you were coming again as a friend after you had been chased away as a colonialist*⁹
 Unkati utithandiza pachuma chidziyenda bwino
You were saying you would help us run the economy well
 Koma chipalanilaneni ubwenziwu chikuchitika n'chiya?
But since this friendship began, what has been happening?
 Udanenanso kuti tisinthe ulamuliro pofunika demokalase anthu azidzilamulira mwau-fulu
You also said that we should change governance for people to rule themselves freely in a democracy
 Molemekezanso wachibadwidwe
*With respect for birth-freedom*¹⁰
 Koma lero akutilamulira ndi nda?
But who is ruling us today?

Pokukukhulupirirani kuti ndinu anzeru
Believing you that you were wise
 Poona kulemera kwa maiko anu
Seeing the wealth of your countries
 Tidatsata ndondomeko zonse za kayendetsedwe ka chuma
We followed every plan of managing the economy
 Ngakhale dongosolo la kamedwe ka mankhwala kuchipatala
Even the plan of administering medicine at hospital
 Koma lero chikuchitika pachuma m'dziko muno n'chiya?
But today what is happening to the economy in this country?
 Pano poti kwalowa njoka udatisasa
*Now that the snake has come you throw us out*¹¹
 Ukuti tikonze kaye njira zathu zoyendetsera chuma
You are saying we should prepare our own ways of managing the economy
 Tikazilongosola ubweranso
When we are putting them in order, you come again
 Tsono apa ukubweranso ukuti tikapanda kuvomereza amuna adzikwatirana
Now that you are coming again, you are saying that if we don't allow men to marry men
 Akazinsu okhaokha sutithandiza
Or women to marry women, you will not help us

⁷ *Chiphamaso* is something that 'kills the eyes' and obscures the true state of affairs. It is commonly translated as 'hypocrisy' by English-speaking Malawians.

⁸ 'Eating a child' (*kudyere mwana*) likens duplicitous friendship to witchcraft (*ufiti*).

⁹ *Mtsamunda* is an established idiom for 'colonialist' and evokes the figure as stealing agricultural land.

¹⁰ *Wachibadwidwe* refers to *ufulu wachibadwidwe*, 'birth-freedom', and is the most common gloss for 'human rights' in Malawi.

¹¹ *Kwalowa njoka*, 'the coming of a snake', expresses an economic downturn and *udatisasa*, 'you throw us out', deploys the verb *kusasa*, which is commonly used for 'brushing off dust' to describe how Malawians are treated during a downturn.

Pakuti tikuphwanya ufulu wachibadwidwe
Because we are violating the birth-freedom
 Chibadwidwe ukunena iwecho ndiye chiti?
*What birth-freedom are you talking about?*¹²
 Ngati ukufuna moyo wathu osangonena bwa?
If you want our life, why don't you just say so?
 Zikakhala ndalama ndi zanu
If it is money, it is yours
 Ife ndalama za nyansi sitikuzifuna
We don't want dirty money

Malingaliro ako pa ife ndi oipa nthawi zonse
Your thoughts on us are bad every time
 Bwanji umatinamiza nthawi zonse?
How come you lie to us every time?
 Ndife osauka inde
Indeed we are poor
 Koma ife siouma mitu
*But we are not dull*¹³
 Malawi walero osauka ali ndi mawu
*Today's Malawi, the poor have something to say*¹⁴
 Paja demokalase udati ndi boma la anthu lochita zomwe anthu akufuna
As you said, democracy is the government by the people to do what the people want
 Koma lero ukufuna bomali lidzichita zofuna nda?
But today who is it that wants the government to meet demands?

Nanga bwanji polimbikitsa za mathanyulazi
And what about when encouraging that homosexuality
 Sukutichenjeza za matenda khumi ndi awiri owopsetsetsawo?
*You did not warn us about the dangerous twelve diseases?*¹⁵
 Bwanji sukutichenjeza kuti tisanayambe kuchita za nyansizi mwaufulu
How come you did not warn us that before we start making that filth freely
 Tiyambe tamanga zipatala za khansa
We should build cancer hospitals
 Ndi kuphunzitsa madotolo ochuluka akadaulo wakhansa wa kotulukira chimbudzi?
*And train several doctors to specialize in anal cancer?*¹⁶
 Kutinso HIV idapezeka koyambirira mwa amuna okhaokha amathanyula 1979
 mpaka 1981
Or that HIV was found only among homosexual men from 1979 to 1981
 Isanapezeke mwa anthu ena
Before it had been found in other people?
 Sukunena zimenezi bwa?
How come you don't say that?

¹²Throughout the poem, the 'you' being addressed is the disrespectful second-person singular *ive*, along with its verbal prefix *u-*.

¹³*Ife siouma mitu* summons the idiom of being 'dry-headed' (*kuuma mutu*) in a denial that Malawians are dull or stupid.

¹⁴*Malawi walero*, 'today's Malawi', alludes to a previous era when poor Malawians were taken for granted by the political elite as acquiescent subjects.

¹⁵*Matenda khumi ndi awiri*, 'twelve diseases', comes from the poet's internet searches and is never detailed in the poem.

¹⁶The poet expresses 'anal' with recourse to *chimbudzi*, a word for both toilet and faeces.

Za anamphulika a ululu ogwira ziwalo za manyazi omwe ukuti azichiritsidwa ku nyansizi
*About the blistering swellings in private parts that you say will be healed through filth?*¹⁷
 Simukunena bwa?
How come you don't say?
 Zoti amuna ochita mathanyula adzayenera kumavalanso matewera
That men doing homosexuality also have to wear nappies
 Ena ataika muzikhwama paulendo kamba ka chimbudzi chomwe chidzangotuluka ngati kasupe
Some they put into a suitcase when travelling for faeces will flow like a fountain
 Bwanji simukunena?
How come you don't say?

Ikadzaphulika miliri khumi ndi iwiriyo pa kamodzi
When those twelve epidemics erupt at once
 Mudzathana nayo bwanji inu mwakonzeka kulowa m'gulu la ochita mathanyulalo?
You who are ready to join the group doing homosexuality, how will you finish them?
 Ndalama sigula moyo m'dzikumbukira
Money does not buy life, remember that
 Lamoyo phukusi umasunga wekha
*The bundle of life, you take care of it by yourself*¹⁸
 Malungo enieniwa akutipha
That big fever is killing us
 Nanga ikabwera miliri khumi ndi iwiri yowopsayo
What about when those twelve serious epidemics come
 Tidzatha bwanji?
How will we manage?

Atithera mudzi mathanyula
Homosexuals finish off our village
 Pobweretsa matenda ovuta kutchula
*By bringing diseases whose names are hard to mention*¹⁹
 Edzi ikuwatha kale anthu m'midzimu
AIDS already finished off people in the villages
 Kulili ikabwera miliri inayi?
What about when the other epidemics come?
 Musadayambe kuchita mathanyula awa fufuzani
Before you have started doing that homosexuality, investigate
 Matenda ena mutalowetse munowa
You will enter other diseases here
 Adzatha dziko lonseli
They will finish off the whole country

Nthawi yokana kukakamidwa kuchita zinthu tsopano yakwana
Time to refuse being forced to do things has now arrived

¹⁷The genitalia are not named in the poem but are expressed through the euphemism *ziwalo za manyazi*, 'embarrassing body parts'.

¹⁸*Lamoyo phukusi*, 'of life, the bundle', deploys a common lyrical device in Chichewa poetry to put the attribute before the noun. In ordinary language, the phrase would be *phukusi la moyo*.

¹⁹*Matenda ovuta kutchula*, 'diseases whose names are difficult to mention', is a euphemism for venereal diseases, such as the 'anal cancer' mentioned earlier.

Ngakhale ndi zovuta koma tingathe
Although it is difficult, we shall be able
 Kuzichotsa unyolo olamuliridwabe ndi azungu ngakhale tili pa ufulu
*To remove the shackles of being ruled by white people even when we have freedom*²⁰
 Ndalama za nyansi sitikuzifuna
We don't want dirty money

Takana mathanyula / We Refuse Homosexuality

Robert Chiwamba

Ndiye inu mukuti bwa? Awo akuti bwa? Iwo akuti bwa?
So, what are you saying? What is that one saying? What are they saying?
 Tonse tikuti takana mathanyula
We are all saying that we refuse homosexuality
 Inuyo mukuti bwanji? Awowo akuti bwanji? Iwowo akuti bwa?
You there, what are you saying? That one there, what is he/she saying? What are those ones saying?
 Tonse tikuti takana utchisi wokwatirana amuna kapena akazi okhaokha
*We are all saying that we refuse the filth of men marrying men or women marrying women*²¹

Dzana munabwera monong'ona kudzatinyengerera
The other day you came quietly to lure us
 Kuti mwabweranso ndi kaufulu kena
*That you had come again with another small freedom*²²
 Kokwatirana amuna kapena akazi okhaokha
Of men marrying men or women marrying women
 Mwina tingakakonde
Perhaps we might like it
 Tinakuuzani
We told you
 'Get out'
Get out
 Utchisi sitimapanga
Filth we do not make

Dzulo munabwera ndi anzathu odziyesa okha ozindikira
Yesterday you came with our friends who think they alone are clever
 Kaya mumati amabungwe omenyera ufulu
You say they are organizations fighting for freedom
 Ufulu wa mimba zawo, za achagogo awo ndi za chakazawo
The freedom of their bellies, of their grandparents and of their wives
 Kudzatiuza kuti mwabwera nawo am'dziko lathu lomwe
To come and tell us that you came with our own compatriots
 Anthu achipala chimodzi omwe akuvomereza zimenezi
*People of the same anvil accepting those things*²³

²⁰ *Unyolo*, 'shackles', associates a contemporary lack of freedom with historical bondage.

²¹ Where Evelyn Pangani uses *nyansi* for 'dirt', Robert Chiwamba's choice, with similar connotations of filth and unhygienic practices, is *utchisi*.

²² *Kaufulu* renders *ufulu*, 'freedom', in the diminutive.

²³ 'Anvil' is the literal meaning of *chipala*, referring here to people of the same mould.

Nafe tisaumiritse mtima
We shouldn't be hard-hearted
 Tinakuyankhani si ife maliro a njoka
We answered to you that we were not without respect²⁴
 Musatitengere kokatiyesa koma mutipulumutse kuzakwaipa muvulala
You should not put us in temptation but you should save us from evil, you get injured²⁵
 Lero ngati sizinamveke mwabwera ndi kamzungu
Today as if it was not clear, you came with a little white person
 Katanyamula chintuwitsa mbali inayi
Who had brought a four-sided scone²⁶
 Kumatiopseza mwati tikapanda kuvomera nyansi zafuluzi
To scare us that if we do not agree with the filth of that freedom
 Anyamula chintuwitsa chake
Helshe will take away his/her scone
 Ndipo tikhaula, tigona ndi njala
And so we will suffer, we will sleep with hunger
 Ife tikuti basopu
We are saying, 'Watch out'²⁷
 'Get out'
 Get out
 Nyamukani inuyo, okumenyerani ufuluwo ndi chintuwitsa chanu
Leave you lot, the ones fighting for that freedom with your scone
 Mudzipita musatitengere kokatiyesa
You must go, you should not put us in temptation

Inuyo mukuti bwanji? Awowo akuti bwanji? Iwowo akuti bwa?
You there what are you saying? That one there, what is helshe saying? What are those ones saying?
 Tonse tikuti takana mathanyula
We all say we refuse homosexuality
 Tawamveni amalawi akuyankhula kumisika, m'maminibasi ndi kumijigo ndi kumababashopuku akuti bwanji?
Listen to them, Malawians are talking in markets, in minibuses, at boreholes and in barbershops, what are they saying?
 Onse akuti mathanyula amawanyansa ngati makhololo a nkhumba
All are saying that homosexuality disgusts them like the pig's phlegm
 Ndithu monga bulu okakamizidwa kutsinje tafika
Indeed like donkeys forced to a river we have arrived
 Koma madzi okha sitimwa madolo
But the water we the brave ones will not drink
 Mbamba ngati mathanyula ali ufulu
I swear if homosexuality is freedom
 Tonse aMalawi tasankha kubwerera kwa Aiguputo kuwukapolo
All of us Malawians choose to return to slavery in Egypt

²⁴ *Maliro a njoka*, 'the snake's funeral', is the fate of those lacking respect and honour.

²⁵ Both 'you should not put us in temptation' (*musatitengere kokatiyesa*) and 'you should save us from evil' (*mutipulumutse kuzakwaipa*) draw on biblical Chichewa.

²⁶ The scone stands for a bribe, and *chintuwitsa* received its name from smearing flour (*kutuwa*) on its eater's lips.

²⁷ *Basopu*, for 'watch out', comes from the Afrikaans *passop*.

Ndithu zotiuza kuti m'chilengedwe chanu

*Indeed to tell us it is natural*²⁸

Kukhala ndi chilakolako kwa mwamuna kapena mkazi mnzanu

To live with a desire among men for fellow men or women for fellow women

Kwa mtu wa galu tatemetsa nkhwangwa pamwala toto

*We refuse in the strongest terms*²⁹

Mbwerera zanu tazimva, utsiru wanu tawuona

Your nonsense we have heard, your foolishness we have seen

Makani anu atikwiyitsa

Your stubbornness has angered us

Taunika chilichonse choyenera kuunikidwa

We examined everything that had to be examined

Tapeza kuti ndi mbwerera, sitingavomere anta

We found it is nonsense, we cannot agree

Kuti ndevu ndi ndevu zipsopsonana, mwikho

*That a beard would kiss a beard, a taboo*³⁰

Sitingalulutire, lipstick ndi lipstick, akupsopsonana, malaulo

*We cannot ululate lipstick kissing lipstick, a bad omen*³¹

Mukauzane kuzipinda kwanu kokambiranako

Go and tell each other in your meeting rooms

Takana mbwerera

We refuse nonsense

Si inu kodi munabwera pa dzana kudzatiuza

Was it not you who came the other day to tell us

Titsatire demokalase

We should adhere to democracy

Ulamuliro wa chigulu?

The rule of the majority?

Lero chigulu chikuyankhula

Today the majority is speaking

Chikuti takana mathanyula

It is saying we refuse homosexuality

Ana m'mwe n'kuti cici? Wewewo akuti cici? Wawodyo akuti cici?

What are you saying? What is that one saying? What are they saying?

Wosope tukanire mathanyula

We are all saying that we refuse homosexuality

Sono imwe mukuti uli? Awo akuti uli? Iwo akuti uli?

You there, what are you saying? That one there, what is he/she saying? What are those ones saying?

Ise tonse tikuti takana mathanyula

*We are all saying that we refuse homosexuality*³²

²⁸ *Chilengedwe* as 'nature' and 'natural' derives from the verb for 'creating', *kulenga*. It refers to all those things, human and non-human, created prior to and independently of any earthly creature's efforts.

²⁹ The poet combines two separate idioms for ardent refusal – *kukanitsa kwa mtu wa galu* (to refuse strongly by the head of a dog) and *kutemetsa nkhwangwa pamwala* (to strike an axe on the rock).

³⁰ *Mwikho* has been adopted into Chichewa from Chilomwe, an endangered language, and its connotations of prohibition are commonly translated as 'taboo' by English-speaking Malawians.

³¹ *Malaulo* is a sign of possible future misfortune and is derived from *kulaula*, a verb for cursing.

³² The previous four italicized lines are in Chiyao and Chitumbuka, languages with large numbers of speakers in southern and northern Malawi respectively.

Choyamba mathanyula ndi tchimo lomwe Yehova, Mphambe, Ngwazi, Chiwothamisi
Firstly, homosexuality is a sin that Jehovah, God, Hero, the Almighty,
 Chilengathambo, Osaodzera, Madalamadala, Kuntunda adana nawo koopsa
The Creator of Clouds, the One Who Never Slumbers, the Elder of Elders, the Top One
*hates profoundly.*³³

Ndipo amatha kulanga ndi osachita nawo omwe bola ngati ali m'dzikolo
And it can punish even those who don't practise it as long as they are in this country
 Ndiye mumabwera ndi timfundo tanu topoyira
So, you come with your small confused ideas
 Ati bwanji inuyonso mumachimwa, kuba, kugona ndi akazi kaya amuna osakhala anu,
 kutamba mkati?
Saying, 'Don't you sin too: theft, sleeping with a woman or a man not your own, bewitching?'
 Koma ndi liti lomwe munamva kuti kutamba kwathu tikufuna kuti kukhale ufulu?
But when did you hear that we want our witchcraft to be freedom?
 Ndikuti ndi liti lomwe munamva kuti umbava ndi uhule wathu tikufuna womerezedwe
 ngati ufulu?
I am saying: when did you hear that our robbery and prostitution should be accepted
as freedom?
 Ndi liti tikuti munamva tikufuna ufulu woyankhula miseche?
When was it, we are saying, when you heard us wanting the freedom of speaking in
swear words?
 'Shut up'
 Shut up

Tonse takana mathanyula
We all refuse homosexuality
 Chachiwiri, mathanyula amatsutsana ndi chikhalidwe cha Chimalawi komanso cha
 umunthu
Secondly, homosexuality is against the Malawian culture as well as humanity
 Ndiye china chimaimika mkono
*And so, a thing raises its arm*³⁴
 Ati 'chikhalidwe chake n'chiti?
Says, 'What is that culture?'
 Azimai athu akumavala maleggingiwa
Our women can wear leggings
 Si chikhalidwe chathu, tilibe chikhalidwe cha Chimalawi ife, osatinamiza'
It is not our culture, we don't have a Malawian culture, don't lie to us'
 Kodi ngati tilibe chikhalidwe chathu
If we don't have our culture
 Unduna wachikhalidwe timakhala nawowa
The Ministry of Culture we have
 Ndi wachikhalidwe cha kuti kapena ku Djibuti?
Is about culture from where or from Djibouti?
 'Foolish'
 Foolish

Tonse takana mathanyula
We all refuse homosexuality

³³The poet's list of God's names does not include the most common one – *Mulungu*. Like *Mulungu* itself, many of the names predate Christianity and Islam.

³⁴The poet places the subject in the class of inanimate nouns.

Chachitatu, mathanyula ali ndi kuthekera kothetsa mtundu wa anthu a m'dziko lathu
Thirdly, homosexuality has the potential to finish the humankind in our country
 Poti ana samabadwa m'menemo
For children are not born in it
 Ndiye chamathanyula china chimafunsa 'mtundu utha bwanji poti ena adzikwatirabe
 amuna kapena akazi n'kubereka ana?'
So, another of the homosexuals asks, 'How does the humankind end when others will still
*marry men or women and give birth to children?'*³⁵
 Kupusa basi, ndani adzikuberekera ana kuti udzipanga nawo mathanyula?
Simply stupid, who would make children for you to do homosexuality with?
 Shupiti
Stupid

Tonse takana mathanyula
We all refuse homosexuality
 Ndiye akumadzakhalanso ndi timfundo tina
So, they also have other small ideas
 Ati 'zochitika pakati pa anthu akuluakulu oti agwirizana kuchipinda zitayeni siziku-
 khudzani'
Saying, 'What happens between consenting adults in a room, let it be, it is not your concern'
 Chiyani?
What?
 Bwanji, mchemwali akagona n'mchimwene wake ngakhale ali aakulu timamanga?
How come we arrest a sister and brother who sleep together even if they are adults?
 Pachifukwa chomwechinso zikutikhudza ndipo awa timanga
Because it concerns us and we arrest them
 Akawamasula, timanganso
When they release them, we arrest them again
 Tikangomva amasulidwanso apolisi athu akawamanganso
As soon as we hear that they have been released again by our police, we go and arrest
them again
 Kungomva mphekesera zoti akutuluka, ife kuwadikirira panja ndi kuwamanganso
To hear only the rumour that they are coming out of prison, we are waiting for them outside
to arrest them again

Njinga saimbira belu pakaliyala
*The passenger does not ring the cycle bell*³⁶
 Malawi asiyerani amalawi apange okha malamulo
Leave Malawians alone to make their laws
 Ndiye kwa inu amabungwe omenyera ufulu wa mimba zanu
And you from the organizations that fight for the freedom of your bellies
 Amene mukumatuma anthu kuti adziyesa zida muwapweteketsa ndipo basobu
You who send people to test weapons to hurt people, watch out
 Osamatiputa dala, kumatiponda zala, potiona ofatsa
*Don't provoke us deliberately, don't step on our toes just because we seem polite*³⁷

³⁵Another of the homosexuals' is again rendered in the class of inanimate nouns.

³⁶The passenger here is a foreigner who tries to control the journey.

³⁷*Ofatsa* translates as 'polite', 'gentle' and 'meek' and questions similar stereotypes about Malawians as in Evelyn Pangani's poem.

Kufatsa *sikupwambana* titha kumenya *mambama*³⁸
 Being polite *is not being stupid*, we can slap
 Timachitira dala, poyesa pokambirana timvana
We try our best to discuss and understand each other
 Koma inu mwati 'zokambirana a-a'
But you say, 'No discussion'
 Koma kumatiopseza 'chithandizo tilanda'
But you threaten us, 'We take away aid'
 Uku mukukisana pambalanganda
*At the same time, you are kissing in the open*³⁹
 Komatu muwasamale anthu akutoperani mafana
Indeed, be careful, people have become tired of you lads
 Ulendo wina sadzakupititsaninso kupolisi anta
Some other time they won't take you to the police, no
 Adzangokuthyolani mphafwa
They will just pierce the liver

Two poems on romantic love

Ngati mawa sindifika / *If I Don't Arrive Tomorrow*

Evelyn Pangani

Lero lino tili limodzipa
Right now that we are together
 Mitima yathu isanadukize m'bebe uwu ukumvekawu
*Before our hearts are broken*⁴⁰
 Dziwa ndimakukonda
Know that I love you

Pomwepa tikulankhulana apa
When we are talking to each other over there
 Dziwa m'mlingaliro mwanga suchoka
Know that you won't leave my thoughts
 Pomwepa tikugwirana zikhathopa
When we are holding each other by the palms of our hands
 Mtima wangawu ukuyambasa iwe
My heart searches blindly for you

Mgundo ukugunda m'mtimamu ndi wachimwemwe chifukwa cha iwe
The heart is beating happiness because of you
 N'katseka masowa mwadala
When I close the eyes deliberately
 Kutsinzina mongothyolera
*Eyes closed, the neck turned to one side*⁴¹

³⁸The italicized words are in Chiyao.

³⁹*Mukukisana* deploys the slang version of 'kissing'. The verb was *kupsopsonana* earlier in the poem.

⁴⁰The imagery is of hearts stopping for a moment because of future suffering already anticipated.

⁴¹*Mongothyolera* alludes to *kutyolera khosi*, 'to lean the neck', a feminine gesture in courtship and flirting.

Chako chithunzithunzi ndicho ndimachiona
Your image is what I see

Kukadzacha tsiku lina ine osadzuka
One sunrise I will not wake up
 Zambiri usadzalire
Do not cry too much
 Chimodzi chokha udzagwetsere msozi
Once only shed a tear
 Ndicho chikondi chakhatakhata tisanuliranachi
This love we pour for each other is thick⁴²

Kuwala kwa dzuwa kokomaku
The sun's beautiful brightness
 Kuomba kwa mphepo ya yaziyazi
The cool breeze blowing
 Sindikumva kukoma ukandikumudwitsa
I won't feel the sweetness if you disappoint me

Pena dziko likamaseka pogirigrishidwa ndi zisudzo achita andalewa
Sometimes the country laughs when tickled by politicians' dramas
 Sizindikomera ukakhumudwa
They don't please me if you are disappointed

Mwina mawa sindifika
Maybe I don't arrive tomorrow
 Chimodzi chokha udzadzitame nacho
Only one thing you should praise yourself for
 Unapangitsako moyo wanga kukoma
You made my life sweet
 Dziko langa unapangitsa kukhala lokwanira
You made my world sufficient
 Ngati mawa sindifika
If I don't arrive tomorrow
 Dziwa unali wanga wapamtima
Know that you were my dearest

Lero lomwe lino tiye kugombe la nyanja
Right now let us go to the lakeside
 N'kakuchengete monga wakowako namwino
I will go and take care of you as your very own nurse

⁴²The imagery is of the lovers pouring a thick substance into each other's containers.

Takumana pano pamsika / We Met Here at the Market

Robert Chiwamba

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndinkamufunitsitsa kwambiri
With a woman I used to desire passionately
 Nayenso adandikondetsetsa koopsa
She too used to be madly in love with me
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying⁴³
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Ndakumana naye ali ndi amuna ake ndi tiana tawo tiwiri
I meet her she is with her husband and their two small children
 Nanenso ndili ndi akazi anga ndi tiana tathu tiwiri
I also have my wife and our two small children
 Akunamizira kuwamwetulira amuna ake chonsecho akumwetulira ine
She is pretending to smile at her husband, all the while smiling at me
 Nanenso kudzanamizira kumwetulira akazi anga pansi pamtima ndikumwetulira iye
I also pretend to smile at my wife, while with all of my heart smiling at her
 Wandiphinyira diso kundilozero amuna ake mwachinsinsi cha mayi
She winks at me to point out her husband to me as a woman's secret
 Nanenso ndamuphinyira diso ndikumulozero akazi anga mwachikondi cha bambo
I also wink at her to point out my wife to her as a man's love
 Pakanakhala kuti palibetu iwo akanandihaga uyu
Had he not been there, she would have hugged me⁴⁴
 Pakanakhala palibe akazi anga ndikanamuhaga uyu
Had my wife not been there, I would have hugged her

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndinkamukondetsetsa kwambiri
With a woman I used to love very much
 Nayenso adandimvetsetsa koopsa
She also used to understand me extremely well
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Ndikukumbukira tinkakulira limodzi padzana
I remember we grew up together in the past
 Ndithu tinkachezera mugulu limodzi ifeyo
Indeed, we used to hang out in the same group
 Ndikadwala ankathamanga kudzandiona ndi kundilimbikitsa
When I fell ill, she used to run to see me and to encourage me

⁴³Chidodo evokes procrastination. Repetition and the pronoun 'I' (*ine*) render it as a self-rebuking exclamation, complete with the suffix *-tu* for the added emphasis on being 'really' slow.

⁴⁴'Hugging' is expressed here as *kuhaga*, derived from English, but the poet also uses the verb *kukumbatira*, adopted from Chiyao, later in the text.

Nayenso zikamuvuta ndinkakhala lake thandizo lopezekeratu
When she also ran into difficulties, I used to be her reliable helper
 Tinkasekererana ndi kusereulana koopsa
We used to make each other happy and to tease each other a lot
 Tinkangokhala ngati chibwenzi
We just used to be like lovers
 Tonse tinkadziwa kuti ndinkamufuna
We both knew I wanted her
 Inenso ndinkadziwa kuti ankandikonda
I also knew she loved me

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndidamuona okongoletsetsa chilengeleni dzikoli
With a woman I have seen to beautify the world since its creation
 Nayenso akundiona owoneka bwino koopsa
She also sees me as extremely good-looking
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Tikufunatu tonse tipeze mpata tiyankhulane
We both really want a chance to talk to each other
 Koma tonsetu mumsika muno talowa ndi achikondi athu
But we both came to the market with our dearest
 Sikuti achikondi athuwa sitimawakonda
It is not that we don't love our dearest
 Koma mtima inu mtima makani nanunso mukudziwa
But the heart, as you know, is a stubborn heart
 Anthu amene tidakondana kuchokera kalekale
People we have loved for a very long time
 Anthu amene tidadziwana kuchokera kusikelo
People we have known since the infant scales⁴⁵
 Mitima yathu ikufuna itasenderanso chifupi
Our hearts want to come closer
 Khutu langa likufuna litamvanso mawu ake
My ear wants to hear again her voice
 Mapiarikaniro ake nawonso akufuna atamva mawu anga
Her ears also want to hear my voice⁴⁶
 Koma musaiwale inu ndi mumsika muno tabweramo ndi okonedwa athu ndi ana athu
But you must not forget that we came to this market with our dearest and our children

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndinkamukondetsetsa kwambiri
With a woman I used to love very much

⁴⁵The imagery is of intimacy arising from knowing each other ever since postnatal health checks.

⁴⁶While the previous line uses *khutu* for 'ear', the word here is *mapiarikaniro*, adopted from Chiyao.

Nayenso adandikondetsetsa koopsa
She also loved me very much
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Tiana tathutu tatsogola tikudutsana tisakudziwana
Our small children are in front and pass each other by without knowing
 Kuti mayi awa ndi ine tikanatha kukhala makolo awo
That this mother and I could have been their parents
 Pakamwa pathu pakufunitsitsa patayankhulana
Our mouths yearn to speak
 Koma tikuyenera kungodutsana ngati sitikudziwana
But we just have to pass by as if we didn't know each other
 Chifukwa panapita nthawi yaikulu tisonaonane
Because a long time has gone since we saw each other
 Komaliza n'kamene anandiimbira lanya ukwati wanga ndi mayiwa n'tamanga
The last time was when she called me on the phone after I had married that woman
 Akulira kundifunira zabwino
She was crying and wishing me well
 Nanenso chaka chimodzi m'mbuyo mwake n'kuti ntalira pomufunira chabwino chi-
 modzimodzi
I also cried a year later while wishing her well in the same way

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndinkamukondetsetsa kwambiri
With a woman I used to love madly
 Nayenso andimvetsetsa koopsa
She also understood me extremely well
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Wanamatu kwa amuna ake ndi kukhulupirira kuti waiwala china chake
She did trick her husband into believing that she had forgotten something
 Si uyu akubwerera wakungofuna kundiona?
Is it not her who is coming back only wanting to see me?
 Nanenso ndikunama kwa akazi anga ndionjezere mayunitsi
I also trick my wife that I need to buy more airtime
 Mwina ndikumana naye
Maybe I will meet her
 Ndakumana naye apayu ndi mkazi amene ndidamukondetsetsa kwambiri
The one I met there is the woman I loved very much
 Akundimwetulira ndipo kuoneka bwino kwake ndi konkuja ngati sanachembezeko
She is smiling at me and looking as good as back then as if she had not aged⁴⁷
 Inenso ndikuoneka bwino lomwe ngati kale
I also look as good as in the past
 Tikukhumba zina zake m'tima mwathu
We yearn for certain things in our hearts

⁴⁷'Ageing' in a woman deploys the verb *kuchembeza*, which means childbearing.

Ndikumuitana m'mene tinkatchulirana kale kuti mbuzi
I call her a goat like we used to name each other in the past
 'Mbuzi iwe n'chifukwa chiyani sunandivomere?'
*'You the goat, why didn't you accept me?'*⁴⁸
 'Mbuzi iwe n'kanavomera bwanji usanandifunsire?'
'You the goat, how could I have accepted before you had proposed to me?'

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndidamukondetsetsa kwambiri
With a woman I loved madly
 Nayenso adandimvetsetsa koopsa
She also understood me extremely well
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Takomedwatu tikukumbatirana ngati simumsika
We get carried away in embrace as if it was not at the market
 Nthawi ikutichepera koma achikondi akudikirira
Time is short for us as our dearest are waiting for us
 Akuliratu mwana wamkazi
She indeed is crying, the female child
 Nanenso sindingapirire misonzi ikulengeza
I cannot prevent either tears from forming
 Sitingapange chibwenzi chaseritu
*We could not have a secret affair*⁴⁹
 Ndife opemphera
We are religious people

Takumana pano ndi pamsika
We met here at the market
 Ndi mkazi amene ndidamukondetsetsa kwambiri
With a woman I loved very much
 Koma sadakhalepo wanga
But she was not to be mine
 Nayenso adandikonda koopsa
She also loved me very much
 Koma sindinakhaleko wake
But I was not to be hers
 Chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 'Mwinatu kudalembedwa anthu okondana zedi asamakwatirane?' akundifunsa
'Perhaps it is written that people who love each other enormously should not marry?'
she asks me

⁴⁸ *Mbuzi* (goat) is normally an insult, but its reciprocal usage here is another indication of egalitarian intimacy between the speakers.

⁴⁹ *Chibwenzi chaseri* is an affair that takes place 'behind the house'.

Pano zaka khumi m'mabanja athu
Now ten years have passed in our families
 Koma timakumbukiranabe tikuuzana
But we tell each other we still remember each other
 Vuto lake mafoni namba sitingagawane
The problem is we cannot share phone numbers
 Tingadzalowe m'kuyesedwa
We could be put into temptation
 Nthawi yatha msanga, make mwana angandifunse mafunso ndikumutsanzika
Our time is finished quickly, my child's mother may ask me questions and I bid her goodbye
 Kulakalaka kumupsopsona
Wanting desperately to kiss each other
 Koma ndangokumbukira ndine dikoni komanso pano ndi pamsika
But I just remember that I am a deacon and here is at the market
 'Tenga handikachifi yanga, nawenso kwaya yangayi uzikandikumbuka ngati sitidzakumananso'
'Take my handkerchief, take it to remember me if we never meet again'
 'Nawenso kachite chimodzimodzi' akundiuzana
'You too do the same,' she is telling me
 Chifukwa chiyani nthawi zambiri Mulungu simumalola anthu omwe tinagwirizana ndi kukondana koopsa
Why so often God does not allow the people we agree with and love very much
 Kuti tikwatirane n'kutipatsa ena m'chikondi chathu?
To marry us but gives us others for our love?
 Koma tikuganizirabe ajawa
But we are still thinking about these ones
 Ajawa mukuwadziwa inu mukuwadziwa
These ones, you know them, you know them

Tinakumana paja panali pamsika
Where we met was at the market
 Ndi mkazi amene ndidamukondetsetsa koopsa
With a woman I loved very much
 Nayenso adandikonda movuta
She also loved me passionately
 Koma chidodotu ine chidodo
But dilly-dallying, my dilly-dallying
 Kupusa ineyo kupusa
Stupidity, my stupidity
 Mkazi ameneyu, tsiku lina, tsiku lina
That woman, some other day, some other day
 Koma inu, tsiku lina
Ah you, some other day
 Ayi zikomo
Ah, thank you